The Baptist Tabernacle of Los Angeles

Mailing Address:
P. O. Box 15308
Los Angeles, CA 90015
Phone: (213) 744-9999
E-mail: rlhymersjr@sbcglobal.net
www.sermonsfortheworld.com
www.baptisttabernacle.com

Dr. Christopher L. Cagan
Pastor

Dr. R. L. Hymers, Jr.
Pastor Emeritus

Disembala, 2020

Okondedwa a Nzanga:

Tadutsa mchaka cha 2020 chimene Satana wasokoneza kwambiri! Pulezidenti kuchotsedwa pa mpando! Kachilombo ka kolona kutikantha! Moto wolusa kuotcha nkhalango zathu za mbiri! Anthu kutsatira ma Komonisiti ndikuchita ngati achita misala, ndi kuotcha mizinda yathu! Ine-ine kulephera kuima kuti ndilalikire! "Ena (anachokako) kuchikhulupiriro, ndikuyamba kumvera mizimu ya zilako-lako, ndi ziphunzitso za chilendo za Satana; kunama mabodza ndi chinyengo; chikumbumtima chawo chitasitidwa ndi moto" (1 Timoteo 4:1,2)! Chingakhale Papa kuvomereza maukwati a amuna okha-okha ndi akazi okha-okha! Zimaoneka ngati kuti dziko lonse likuphulika; Yesu anati,

> "Ndipo kudzakhala zizindikiro pa dzuwa ndi mwezi ndi nyenyezi; ndi pa dziko lapansi chisauko cha mitundu ya anthu, alinkuthedwa nzeru pa mkokomo wake wa nyanja ndi mafunde ake; anthu akukomoka ndi mantha ndi kuyembekezera zinthu ziri nkudza kudziko lapansi; pakuti mphamvu za kumwamba zidzagwedezeka. Ndipo pamenepo adzaona mwana wa munthu alinkudza mu mtambo ndi mphamvu ndi ulemerero waukulu. Koma poyamba kuchitika izi weremukani, tukulani mitu yanu; chifukwa chiomboledwe chanu chayandikira" (Luka 21:25-28).

> "Koma mudzaperekedwa ngakhale akukubalani, ndi a bale ndi a pfuko lanu, ndi abwenzi anu; ndi ena a inu adzakuphani" (Luka 21:16).

Tingawerenge bwanji ndime zimenezi ndikusadziwa kuti tiri m'masiku otsiriza a mu ulosi wa Baibulo?

"Koma ndi nthawi ya Khrisimasi," mukutero! Mu Disembala wa 1941 Churchill anali kuno kochoka ku Mangalande chifukwa kunali koti ma Japani anali ataphulitsa bomba pa doko la pa Pale ndipo Hitira amaphulitsa London. Churchill anali mnyumba ya chifumu yaku Amereka ndi Pulezidenti Franklin D. Roosevelt. Pamene pulezidenti anayatsa mtengo wa Khrisimasi wa dziko, Churchill anati, "Aloleni ana akhale ndi usiku wa chisangalalo ndipo asewere."

Koma inu ndi ine sindifenso "ana" ayi! Iyi ndi nthawi yozindikira kuti chiyembekezo chathu chagona pa khanda, lobadwa mu Yerusalemu – ndipo sitiri ndi chiyembekezo cheni-cheni koma cha kubweranso kwa chiwiri kwa Yesu ngati Mfumu ya ma Fumu ndi Mbuye wa Ambuye!

Kalero, cha mzaka za m'ma 1960, Mulungu anandipatsa vesi limene landithandiza kwambiri ngati mbusa m'masiku ano otsiriza.

> "Ndikhonza zonse mwa Iye wondipatsa mphamvu" (Afilipi 4:13).

MUKHONZA KUWERENGA ZIKWI-ZIKWI ZA MA ULALIKI NDI ZIPHUNZITSO ZATHU MU ZILANKHULO MAKUMI ANAYI NDIASANU PA WWW.SERMONSFORTHEWORLD.COM.

Pa Febuluwale 2 timakumbukira chaka cha tsopano cha a Chaina nthawi ya mapempero athu a kum'mawa ndi kumadzulo. Marichi 1 linali la Mulungu lotsiriza tinakumana mnyumba ya kale yomwe yiri ku msewu wa ku Hope. Mchaka chonsechi cha (2020) takhala tikukumana mnyumba ziwiri, chifukwa cha kolona. Sabata iriyonse ndimajambula kanema wa chiphunzitso, chomwe chimaonetseredwa mnyumba ziwiri zimenezi. Tikatha kumva chiphunzitso cha pa kanemachi timakha ndi mgonero.

Tsiku lokumbukira kubadwa kwanga la chi 79 linali pa Apulo 12, la Mulungu loyera. Anakumbukira kubadwanso kwa mkazi wa Hymers pa Epulo 16. Ndikhonza kunena kuti, "Ana akazi ambiri anachita mwa ngwiro, koma iwe uposa onse" (Miyambo 31:29).

Pa Septembala 27, mpingo umakumbukira kuti tatha za 38 mbanja. Chaka chathachi ndakhala ndikubvutika nthenda ya m'mimba, imene inandisautsa kuti ndiyime kulalikira. Chinali chiyambi cha khansa amene anayamba kuononga mitsempha zomwe zinayambitsa nthenda imeneyi.

Komabe, chaka chomwechi, Mulungu wadalitsa ntchito yathu! Taonjezera zilankhulo zina zitatu za ziphunzitso za vesi ndi vesi za Baibulo ndi ma ulaliki pa tsamba lathu la intaneti pa www.sermonsfortheworld.com. Taonjezera Khongso Chin, chilankhulo cha ku Myanmar (Burma) ngati chilankhulo chathu cha chi 43. Tinaonjezeraponso Malayalam, chilankhulo china cha ku India, ngati chilankhulo cha chi 44. Komanso tinaonjezera Sinhala, chilankhulo cha ku Sri Kanka, ngati chilankulo cha chi 45.

Ndimalandira ma email ambiri sabata iriyonse kuchokera kwa a laliki osiyana-siyana, ondiuza m'mene ziphunzitso ndi ma ulaliki akuwathandizira.

Pa Julaye 7 nyumba yathu ya kale imene ili mu msewu wa Hope inalipiridwa, tikuthoza mwanawathu Robert chifukwa cha zomwe anachita.

Pa October 13 mpingo wonse unasangalalira moyo wa Bambo Eugene Grace pa mwambo umene unachitikira pa manda a Riverside. Dr. Cagan anali atango walandilitsa Yesu m'maola ochepa asanamwalire ali ndi za 91. Bambo Grace anali bambo wake omupeza a Tom Xia, mnyamata wokhazikika wa mu mpingo wathu. Patapita masabata awiri, Dr. Cagan anakapereka uthenga wabwino kwa mkazi wa bambo Grace, Sophie, tsopano maiwa ali ndi moyo wosatha. Ndiri ndi chikhulupiriro kuti akhala woyamba kubatizidwa ku malo athu atsopano a San Gabriel. Mkazi wa Hymers anapita ku Riverside kukakhala nao pa mwambo wa maliro wa bambo Grace. Kenaka anandiyendetsa kupita ku Oxnard, kumene tinakakhalako masiku awiri kupuma mphepete mwa Nyanja.

Pa November 22 (Lamulungu) tidzakhala ndi mwambo wothokoza kunyumba kwa Dr. Cagan ku Alhambra.

Ndikanagwirabe ntchito, yolemba ziphunzitso ndi ma ulaliki, ndikumathandiza Dr. Cagan. Mu masabata angapo ukubwerawo, ndi mzaka 81 za moyo wanga. Sindikanapitiriza kugwira ntchito popanda mkazi wanga wokondedwa, Ileana – ndi Yesu kumene kumachoka mphamvu zanga kuti ndizipitirira kumtumikira.

"Ndikhoza zonse mwa Iye wondipatsa mphamvu" (Afilipi 4:13)

Iri ndi lonjezo la Yesu! Ndimaliza kalatayi pa kupereka umboni woperekedwa ndi amane ndimagwira naye ntchito, Dr. Christopher L. Cagan:

> Mzaka za mbuyomo ndinalibe mtendere. Ndinkakhala moyo wa ine ndekha. Sindinkaganizira za Mulungu kapena kulabadira zimene zidzachitike ndikadzafa. Ndimadzidalira ndekha. Ndinkathawa-thawa ndi kumuzembera Mulungu. Kusukulu ndinkakhoza bwino kwambiri ndipo ndimalandira ndalama za mbiri, koma ndinali ndekha wosasangalala.
>
> Kenaka ndinakumana ndi a Kristu ena amene anali abwino kwa ine. Ndinayamba kupita ku Tchalichi. Komabe ndinkafuna kuyenda njira ya ndekha. Usiku wina ndinapita kukasonkhana ndi a nzanga pa sukulu. Mnyamata wina anandiuza nkhani yabwino yomwe sindinaimvepo chikhalire – yoti Mulungu amandikonda ndipo akufuna kundipatsa moyo wosatha. Anandiuza m'mene ndingapezere moyo umenewo. Usiku umenewo ndinamudalira Yesu. Anandikhululukira machimo anga nandipatsa moyo wosatha.

Tsopano ndiri ndi mtendere. Tsopano ndiri ndi moyo wosatha. Yesu anadichiza mkati mwanga. Anandipatsa chiyembekezo ndi chimwemwe. Sindiri ndekhanso ayi. Ndikudziwa kuti nditafa usiku uno, ndikakhala ndi Mulungu Kumwamba, chifukwa Yesu wandipatsa moyo wosatha!

Ndiri wosangalala kuti ndikumutumikira Yesu! Sindikanatha izi popanda mphamvu Zake ndi chisomo, komanso opanda Dr. Cagan, Ileana, ndi mwana wathu John Wesley, amene akaphunzire za magazi ndi maphunziro ena ofafana ndi za magazi.

Yesu akudalitseni ndi banja lanu! Chonde pempherani Kent Philpott ndi ine, pamene tikusanthula buku limene akulemba Kent la kumasulidwa mdzina la Yesu! Chonde tipempherereni ife ngati mpingo pamene tikuyambiutsa mpingo wina wa Chinese Baptist ku San Gabriel.

Dr. Hymers ndi Mkazi wake Ileana, mwana wake Robert, mkazi wa Robert Jin, ndi tiana tatikazi ta Robert Hannah ndi Sarah. Ndikupemphera kuti akhalenso ndi khanda lina mosachedwapa.

Kristu alemekezedwe nthawi zonse!

Rev. R. L. Hymers, Jr.,
D.Min., D.Rel., Th.D., Litt.D.
Afilipo 4:13

"Munthu wosochera pa njira ya nzeru adzakhala m'sonkhano wa akufa" (Miyambo 21:16).

MUKHONZA KUWERENGA ZIKWI-ZIKWI ZA MA ULALIKI NDI ZIPHUNZITSO ZATHU MU ZILANKHULO MAKUMI ANAYI NDIASANU PA WWW.SERMONSFORTHEWORLD.COM.